# ULIMI WA MITENGO

## Malangizo a alimi ang'ono-ang'ono a m'mag-ulu

### Kodi nasale n'chiyani?

Nasale ndi malo pamene amabzala kapena kufesa mbewu zing'ono-zing'ono za mitengo mpaka zitakula/zitafikapo kukazibzala pamalo oyenelela. Kulima mbewu pa nasale coyamba kumapeleka mwayi waukulu wakuti zipulumuke. Pamakhalanso mwayi wosankha mbewu zabwino zimene zingabale zipatso zabwino m'munda.

### Malangizo a mosamalila nasale

Ganizilani izi pokonza nasale ya mitengo:

▶ **Mitundu ya mitengo** – monga mlimi muyenela kudziwa n'chifukwa chiyani mwasankha mtengo umenewo. Chidziwitso chimenechi chidzathandizila m'mene mungapelekele chisamalilo ndi kuyanganila. Mfunseni mlimi wotsogolela/wankulu kapena nyanchito wothandizila alimi pa zamapindu a mitundu-mitundu ya mitengo. Osabzala mtengo chifukwa cha pulojekiti chabe kapena aneba akuuzani zimenezo.

▶ **Nambala ya mbewu ndi tumitengo tofunika pa malopo:**

- Ganizilani malo osiyana-siyana pozabzala mitengo mtsogolo: pafupi ndi nyumba, mudimba kapena munda wanu.
- Ganizilani za mtundu wa mtengo mudzabzala pa malo ati. Onetsetsani kuti malo alipo.
- Onetsetsani kuti mudzatha kunyamula mbewu zanu n'kukabzala pamalo kapena m'malo angapo.
- Mudziwitseni mlimi wotsogolela pa zofuna zanu.


*Promotion of agroforestry*

*Supported by:*

unique land use

With support from Federal Ministry of Food and Agriculture by decision of the German Bundestag

ONE ZAMBIA ONE NATION

Prepared by: Daniel M. Kalala; Graphic design: Jonathan Leya


## Ndondomeko yopangila nasale ya mitengo

1



**Kukonzekeletsa malo –** pamalo payenela kukhala: (i) mum'thunzi; (ii) posavuta kufikapo; (iii) pafupi ndi madzi; (iv) potetezeka ku zinyma (pomangila); (v) pamalo olimidwa, palibe udzu, zitsamba kapena zulu.

2



**Kusankha mbewu –** sankhani mbewu kuchokela ku chipatso kapena nsale ilibe matenda, yakupsa yokhwima. Njele zisungidwe pamalo ouma & pakuda musanabzale/kufese.

3




**Kukonzekeletsa malo olimapo –** sakanizani mbali 3 za dothi ya nthaka, mbali 2 za dongo/katondo, mbali 1 ya manyowa ndi 1 ya mchenga. Thililani pang'ono lelo kuti mawa mudzaike m'mapulasitiki

4

| | Pre-treatment method |
|---|---|
| Gliricidia | Viikani/kunyowetsa usiku wonse ndi kubzala m'mawa mwake |
| Mango | Dulani njele pang'ono ndi mpeni, viikani masiku 3 -4 n'kufenda chikoko chake. |
| Ndimu/lemons | Kuviika usiku wonse n'kufenda chikoko m'mawa mwake |
| Papaya | Kuviika usiku wonse, kubzala m'mawa mwake |
| Moringa | Kuviika usiku wonse kubzala m'mawa mwake |
| Khaya (Mubaba) | Kufenda chikoko cha njele, n'kuviika usiku wonse |
| Tephrosia | Kubzala mwachindunji (osakonza nasale) |
| Pigeon pea | Kubzala mwachindunji (osakonza nasale) |
| Neem | Bzalani ukali wauwisi kapena masiku angapo mutakolola |

**Kukonzekeletsa Mbewu –** Mtundu ulionse wa mbewu umasamalilidwa mosiyan monga mwaonela pamwambapa.

5



**Kubzala -** bzalani mbewu kulowa pansi kutalika kokwanila ngati 1 kapena 2 mu ufupi wa mbewuyo. Bzalani mbewu imodzi m'palasitiki imodzi. Yambani kudzadza mapulasitiki amenewa n'dothi mu kuyambila September. Bzalani njele za mitengo ikula mochedwa kuchiyambi kwa October. Bzala njele za mitengo ikula mwam'sanga monga Gliricidia kothela kwa October kapena kuchiyambi kwa November.

6



**Kuphimbila, kuthilila & kulimilila -** phimbilani mapulasitiki pambuyo pobzalamo mbewu. Thililani kawili pa tsiku - m'mawa komanso m'madzulo. Kuthilila mbewu kawili-kawili pa mulungu kudzadalila mnyontho uli m'nthaka mu pulasitiki.

7



**Chitetezo cha tomela tung'ono-tung'ono**:

(I) Ku ziweto – mangani mpanda/fensi
(ii) Ku moto - pasakhale udzu wouma pafupi ndi tomela n'kubukitsa moto. Pangani m'mbali momwe moto udzafike/thele kuzungulila nasale.
(iii) Ku chiswe - gwilitsilani nchito mankhwala ophela tulombo monga snake beans, tephrosia kapena phulusa. Wazani mankhwala amenewa ponse pali mbewu zomela zikulimidwa.

8




**Kudulila mizu:** iyi ndi njila yosamalila kakulidwe ka mizu kuti isakule kutuluka muthumba ya pulasitiki. Kuchita zimenezi kumathandiza: (i) Mizu isakule n'kulowa pansi; (ii) kulimbikitsa kukula kwa mizu yodyetsela; (iii) mizu ya mbewu kukula pang'ono-pang'ono. Mungaletse mizu kutalika mwa kuika mbewu pa pulasitiki (A); kapena kudula mizu ikutulukila pabwalo pa thumba ndi sizala kapena mpeni (B); kapenanso kuika pulasitiki mobzala pokwezeka (C).

9



**Kulimbitsa Mbewu –** iyi ndi njila yothandizila zomela zing'onozing'ono kuti zilimbe kuti m'kupita kwa nthawi zikakwanitse kukhala mu nyengo yakuchile. Zimenezi zimapewetsa kuwonongeka kapena kufa kwa tumitengo mwa kutubweletsa ku nyengo yakuchile pang'ono-pang'ono. Pakati pa masiku 7 ndi 10 musanafike pa tsiku yokabzala, chepetsani madzi mwa kuthilila kamodzi pa tsiku pambuyo pake kamodzi pamasiku awili.

**Kagawidwe ka mbewu:** gawilani mbewu za tumitengo kwa mamembala a kagulu ka alimi pamene mvula yayamba kugwa bwino. Ichi chimapeleka mwayi wakuti mitengo ikule bwino. Ngati membala m'modzi wakana kutengapo mtundu wa mbewu ina, mbewuyo idzagawidwa ku mamembala onse molinganiza.

**Samalani podulila mizu:** kudulila mizu sikuyenela kuchitika milungu iwili musanayambe kubzalila/kufe mbewu chifukwa tumitengo kulalibe kuchila bwino-bwino. Pambuyo podula mizu, tumitengo tuyenela kuthililidwa chifukwa tungakhale topanikizika.